# Malongosoledwe a coonadi ca m'Baibulo

**Za moyo wa Yesu wa pa dziko lapansi**

1. Yesu anadza kucokera Kumwamba
2. Yesu anamvera Mulungu
3. Yesu anali Mphunzitsi
4. Yesu analetsa mphepo ndi nyanja
5. Yesu analetsa matenda ndi imfa
6. Yesu anakhululukira macimo
7. Yesu anaonetsa m'mene aliri
8. Yesu anaonetsa ulemerero wake

Koma zalembedwa izi kuti mukakhulupirire kuti Yesu ndiye Kristu Mwana wa Mulungu, ndi kuti pakukhulupira mukhale nao moyo m'dzina lace – Yohane 20.31

Mbali zina za m'buku iri zinasandulidwa kucokera ku buku ilo: Schoolland, Marian. M. (1962), *Leading Little Ones To God* (21st ed), Wm. B. Eerdmans Publishing Company.

- ©Stephanos Zambia Trust –
www.kudziwazamulungu.com

## 1. Yesu anadza kucokera Kumwamba

*Cifukwa ca inu* (Yesu Kristu) *anakhala wosauka, angakhale anali wolemera - 2 Akorinto 8.9b*

**Kuwerenga**
Yohane 3.16 ndi 17

**Malongosoledwe**
Kodi mudziwa pamene moyo wanu unayamba? Inde, unayamba pamene munabadwa. Caka ciriconse tiri ndi tsiku lokumbukira kubadwa kwathu. Amai amakumbukira bwino tsiku lomwelo. Pa nthawi iyo munali mwana wankhanda, mwana wokondedwa wankhanda.
Yesu anabadwanso ngati Mwana wankhanda. Koma Yesu sanayambe kukhala moyo pa nthawi ya kubadwa kwake. Yesu anakhala moyo asanabadwe Iye. Yesu ndi Mulungu ndipo Mulungu alipo nthawi zonse. Yesu, Mwana wa Mulungu, anakhala Kumwamba pamodzi ndi Mulungu Atate ndi Mulungu Mzimu, kale-kale dziko lapansi lisanalengedwe.
Mukumbukira kuti dziko lapansi linali labwino ndi lokongola pa ciyambi. Adamu ndi Hava anali odabwitsa; anapangidwa m'cifaniziro ca Mulungu. Koma uchimo unabwera naononga zonse. Mulungu anamva cisoni pa zowawa ndi mabvuto amene anabwera kucokera pa nthawi iyo. Ndipo Mulungu anati, 'Ndidzatuma Mpulumutsi'. Ndipo Yesu anati, '*Ine* ndine wofuna kupita pa dziko lapansi ndi kukhala Mpulumutsi!' Mzimu Woyera anapanga thupi la Yesu. Ndipo Yesu anabadwa ngati Mwana wankhanda. Anabadwa m'Betelehemu. O, angelo anaimba bwino usiku womwewo – khamu la angelo! Anakondwera kwambiri kuti Yesu anadza pa dziko lapansi. Anakondwera pakuti Yesu anapita kukhala Mpulumutsi wathu.
Kunali kusintha kwakukulu kwa Yesu: anasiya Kumwamba nadza pa dziko lapansi. Mwamba ndi wodzala ndi ulemerero. Kulibe matenda, cisoni kapena uchimo. Koma Yesu anasiya Nyumba yake yokongola ndi Atate wake ndi angelo odabwitsa nabwera pansi pano pa dziko lathu lapansi locimwa.
Yesu anali *wolemera* Kumwamba; zonse zinali zake. Pobwera pa dziko lapansi, Iye anali wosauka. Anasiya cuma conse ndi ulemerero wonse. Kunalibe ngakhale nyumba yokonzedwa ya Iye pa dziko lapansi. Anabadwa m'khola. Ndipo analibe bedi. Mai wake Mariya anamuika m'gome lodyeramo nyama.
Yesu anali *wamphamvu zonse* Kumwamba. Anali Mbuye wa kumwamba ndi dziko lapansi ndiponso Mbuye wa angelo onse. Pamene anasanduka Mwana wankhanda, Iye analibe mphamvu iriyonse! Ana ankhanda afunika amai kuwasamalira. Yesu anakhala pukulu monga ana ankhanda onse.
Yesu anasanduka kukhala ngati ife, komabe Iye analibe uchimo m'mtima mwake monga ife tiri nawo pamene tinabadwa.
Nthano ya kubadwa kwa Yesu ndi yodabwitsa koposa m'Baibulo. Ndi yodabwitsa koposa pa dziko lonse lapansi ndi m'Mwamba. Ganiziraniko: Yesu, Mwana wa Mulungu anasanduka Mwana wankhanda!
Anasanduka Mwanu kukhala Mpulumutsi wathu, pakuti Mulungu atikonda kwambiri nafuna kutipulumutsa.

**Kukambirana**

1. Kodi Yesu anali kuti asanabwera pa dziko lapansi?
2. Ndi cifukwa ciani Yesu anadza pa dziko lapansi?
3. Kodi Yesu anasiya ciani Kumwamba?
4. Kodi mukumva bwanji pa zimene Yesu anacita?
5. Kodi Yesu ndi Mpulumutsi wanunso?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wa Kumwambamwamba, Tikuyamikani kuti munatuma Mwana wanu pa dziko lapansi. Ambuye Yesu Kristu, tikuyamikani kuti munali wofuna kusiya Kumwamba ndi kukhala Mpulumutsi. Mulungu Mzimu Woyera, tikuyamikani kuti munapanga thupi la Yesu kuti abadwe pa dziko lapansi. Tiphunzitseni kukukondani koposa. M'dzina la Yesu tikupemphani izi. Amen.

## 2. Yesu anamvera Mulungu

*Ndipo popezedwa m'maonekedwe ngati munthu, anadzicepetsa yekha, nakhala womvera kufikira imfa, ndiyo imfa ya pamtanda – Afilipi 2.9*

**Kuwerenga**
Mateyu 1.1-11

**Malongosoledwe**
Kodi mudziwa dzina la mwamuna woyamba wolengedwa ndi Mulungu? Kodi mukumukira dzina la mkazi woyamba? Mudziwa kuti Adamu ndi Hava anakhala m'munda wokongola. Zonse zinali zokongola ndipo iwo anasangalala kwambiri mpaka tsiku la kusamvera Mulungu.
Cifukwa ciani iwo sanamvere Mulungu?
Mulungu ali ndi mdani. Satana ndi mdani wa Mulungu. Akuda Mulungu. Satana anayesa Adamu ndi Hava. Anawapangitsa kucimwira Mulungu. Iye anakondwera pamene iwo sanamvere Mulungu.
Pamene Yesu anakhala pa dziko lapansi, Satana anamuyesanso kuti asamvere Mulungu. Baibulo litiuza momwe Satana anayesa Yesu.
Satana anatenga Yesu kunka naye ku cipululu (ndico monga nkhalango yopanda anthu). Anamuyesa Yesu masiku makumi anai kuti Yesu angakhale wosamvera Mulungu. Cinali cobvuta kwa Yesu kunena 'iai' kwa Satana nthawi zonse.
Potsiriza, pa tsiku labwino, Satana anatenga Yesu naye pamwamba pa phiri lalitali kwambiri. Iwo anakhoza kuona patali naona zonse zowazungulira. Satana anaonetsa Yesu minda yonse yaikulu ya pa dziko lapansi, nyumba za mafumu zooneka bwino ndi golide ndi siliva ndipo anaonetsanso mafumu ndi ana ao ndi magulu a asirikali.
'Izo zonse ndi zanga', Satana ananena. 'Koma zonse ndikupatsani Inu, ngati mudzagwa pansi ndi kundigwadira ine'.
Yesu ananena, 'Coka, Satana! Pakuti Baibulo likamba kuti tizipembedza cabe Ambuye Mulungu wathu'.
Yesu sangacite cifuniro ca Satana. Yesu sangakhale wosamvera Mulungu.
Yesu anakonda Mulungu Atate. Anamvera Mulungu. Tsiku ndi tsiku, kucokera m'mawa kufikira usiku, Yesu anamvera Mulungu. Sanacite coipa nthawi zonse. Ngakhale pamene anali Mnyamata wamng'ono, Iye sanacite mwano. Ndipo anamveranso Mulungu ngakhale podzipereka pa mtanda kutifera.
Adamu ndi Hava sanamvere Mulungu. Mukumbukira nthano: iwo anacita cimene *iwo* anafuna, osati cimene Mulungu anawauza kucita. Ndipo ife nthawi zambiri-mbiri ticita zimene *ife* tifuna m'malo mwa kucita zimene Mulungu afuna. Koma Yesu anamvera nthawi zonse. Iye anati kwa Atate wake, 'Osati cifuniro canga, koma cifuniro canu cicitike'.
Yesu anamverera kubwezera kusamvera kwathu. Anayenera kukhala womverera kuti akhale Mpulumutsi wathu.
Ndipo tsopano, ngati tikonda Yesu, tidzayesa kwambiri kopambana kukhala omvera. Tidzayesa kucita zonse zimene Mulungu afuna kuti tizicita. Tifuna kucita cifuniro cake.
Nthawi zina kucita cifuniro ca Mulungu kungakhale kobvuta. Koma Mulungu adzatithandiza. Anathandizanso Yesu. Pamene Satana anacokapo, Iye anatuma angelo kutumikira Yesu.

**Kukambirana**
1. Ndi yani amene anayesa Yesu kodi?
2. Kodi Yesu anaonetsa bwanji kuti aika Mulungu patsogolo?
3. Nanga inu, muika cifuniro ca Mulungu patsogolo?
4. Kodi timvera moonadi ngati munsi m'mtima mwathu sitifuna kumvera?
5. Kodi tikwaniritsa kucita cifuniro ca Mulungu nthawi zonse?
6. Kodi tiyenera kucita ciani ngati tiyesedwa kusamvera Mulungu?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Mulungu wamkulu, Ife tilakwa kawiri-kawiri kukumverani. Sitikwaniritsa kucita cifuniro cathu. Mudziwa macimo athu onse. Mutipulumutse kuti tizicita cifuniro canu ndi kulondola Yesu Kristu amene anali womvera. Tithandizeni kupewa mayesero ndi kukulemekezani nthawi zonse. M'dzina la Yesu Kristu tapempa izi. Amen.

## 3. Yesu anali Mphunzitsi

*Simoni Petro anamyankha Iye, Ambuye, tidzamuka kwa yani? Inu muli nao mau a moyo wosatha – Yohane 6.68*

**Kuwerenga**
Mateyu 5.1-8

**Malongosoledwe**
Yesu anadza kukhala Mpulumutsi wathu. Koma anadzanso kukhala Mphunzitsi wathu.
Yesu sanaphunzitse ku sukulu. Anaphunzitsa pabwalo. Nthawi zina anakhala pa phiri, pali udzu, ndipo anaphunzitsa anthu okhala pafupi naye. Nthawi zina anakhala m'ngalawa pa nyanja ndipo anthu amumvera anakhala pa mbali pa nyanja. Nthawi zina anakhala pa khonde la Nyumba ya Mulungu nalankhula ndi anthu amene adabwera kupembedza Mulungu. Ndipo nthawi zambiri pamene Iye anayendera m'mzinda kapena pa njira, anthu anayenda naye ndipo Iye analankhula nao pamene anayenda pamodzi.
Yesu sanaphunzitse anthu kulemba ndi kuwerenga. Anaphunzitsa cinthu cofunikira kwambiri koposa: kudziwa Mulungu. Anauza anthu za cikondi ca Mulungu. Anawathandiza kuona kuti m'kati mwa mtima mwathu muli uchimo woipa kwambiri. Anawauza kuti adadza kufa cifukwa ca macimo athu, kuti tikhale ana a Mulungu. Anawauza za cilango ca kwa anthu onse amene samvera Mulungu. Ndipo anawauza za dziko lapansi latsopano limene Mulungu adzapanga, dziko lopanda chimo lirilonse.
O, anthu anakonda kwambiri kumvera Yesu. Anamtsata paliponse pomwe anapita. Nthawi zina anthu zikwi anakhala pa phiri pamene Yesu anawaphunzitsa za Ufumu wa Kumwamba.
Ana ang'ono anakondanso kumvera. Nthawi zina Yesu anawatenga pafupi naye. Ndipo anawakhumbatira. Anawakonda.
Makamaka anthu osauka, anthu odwala, anthu osiyidwa ndiponso iwo odziwa kuti ndiwo ocimwa kwambiri anakonda kumva Yesu. Iwo anaganiza kuti kulibe munthu wina aliyense amene awakonda, koma anaona kuti Yesu awakonda. Yesu anawauza kuti ayenera kupereka mtima wao kwa Mulungu ndi kuleka kucimwa. Ndipo iwo poona m'mene Yesu anawakonda, sanafunebe kucimwa.
Kodi mufuna Yesu kukhala Mphunzitsi wanu? Iye adzakhala Mphunzitsi wanu ngati muwerenga mau ake m'Baibulo. Ndipo Iye ndi Mphunzitsi wanu ngati muwerenga nthano za m'Baibulo. Iye ndi Mphunzitsi wanu pamene mupita ku calichi kapena ku sukulu ya ana ang'ono kuphunzira za Mulungu. Cifukwa pamenepo aziphunzitsi ndi azibusa akuuzani mau a Yesu. Ndipo mau awa ndi odabwitsa.
Petro anali m'modzi wa ophunzira a Yesu. Anayenda naye tsiku ndi tsiku ndi kumumvera. Anadziwa kuti kale kunalibe Mphunzitsi wodabwitsa kotere.

Tsiku lina Petro anati kwa Yesu:
*Inu muli nao mau a moyo wosatha.*

**Kukambirana**
1. Kodi Ambuye Yesu anaphunzitsa ciani?
2. Ndi cifukwa ciani Ambuye Yesu anali Mphunzitsi wopambana?
3. Kodi mufuna Yesu kukuphunzitsani? Ngati iai, ndi cifukwa ciani mwayankha tero? Ngati inde, mufuna kuti akuphunzitsani ciani?
4. Ngati Yesu atiphunzitsa, ife ndife ophunzira. Kodi kukhala ophunzira a Yesu kutanthauza ciani?
5. Kodi mumacita ciani kuphunzira zina za Mulungu?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wa Kumwamba, Tikuyamikani kuti munatuma Yesu kukhala Mphunzitsi kutiphunzitsa mau a moyo. Tithandizeni kumvera pamene tikumva Mau anu ndi kusunga Mau anu m'mtima mwathu. Tikupemphani izi mwa cisomo, m'dzina la Yesu. Amen.

## 4. Yesu analetsa mphepo ndi nyanja

*Ndipo iwo anacita mantha akuru, nanena wina ndi mnzace, Uyu ndani nanga, kuti ingakhale mphepo ndi nyanja zimvera Iye? – Marko 4.41*

**Kuwerenga**
Marko 4.35-41

**Malongosoledwe**
Nyanja ya Galileya ndi nyanja yaikulu ndi yokongola. Yesu anakonda kuyenda pafupi ndi nyanja. Ophunzira ake anayenda naye. Yesu anawauza zambiri za Mulungu pamene anayenda pamodzi nao.
Tsiku lina anthu ambiri anabwera kumvera Yesu. Yesu anati kwa Petro, 'Ika ngalawa yako pa madzi. Ndidzakhala pansi pa ngalawa ndipo anthu akhoza kundimvera ku mbali ya nyanja.'
Anthu anakonda kumvera Yesu. Anakhala pa mbali ya nyanja tsiku lonse pomumvera. Pamene usiku unayamba, iwo anapita kunyumba. Ndipo Yesu analema.
Yesu anati kwa ophunzira ake, 'Tiyeni tipite tsopano ku mbali ina ya nyanja'.
Ophunzira ndi Yesu anapita m'ngalawa. Anakweza nsalu yoyendetsa bwato ndipo anapita pa nyanja. Yesu anakhala pansi pa mtsamiro nagona. Analema kwambiri.
Mbali ina ya nyanja inali kutali. Kunada. Usiku unabwera. Ndipo ophunzira anali kuyendetsabe ngalawa.
Ndipo kenaka mphepo inayamba kuomba kwambiri. Mphepo inapangitsa mafunde owaza madzi m'ngalawa. Ophunzira anatsika nsalu. Anaopa kuti ngalawa ingagubuduke. Anayamba kupalasa ngalawa koma sanakwaniritsa kuyenda bwino cifukwa ca mafunde akulu. Ndipo Yesu anali kugonabe!
Ophunzira anayesa kwambiri kuyendetsa bwato ku mbali ya nyanja. Koma sanakhoze kufikako. Ndipo ngalawa inayamba kudzala ndi madzi. Ophunzira anaganiza kuti adzamira m'madzi.
'Tiyenera kuukitsa Yesu!', iwo anati. Ndipo anayamba kumuitana. 'Ambuye! Ambuye! Ukani! Kodi simusamala kuti titayika ife?'
Yesu anatsegula maso ake. Anakhala naona mafunde. Anamva mphepo yoomba pa nkhope yake. Ndipo anaona ngalawa yodzala ndi madzi.
Koma *Iye* sanaope.
Anaimirira pa ngalawa. Anayamba kulankhula kwa mphepo ndi mafunde. Anati, 'Tonthola, khala bata'.
Ndipo mwadzidzidzi mphepo inaleka kuomba. Ndipo mafunde analeka kuwaza madzi!
O, ophunzira anadabwa kwambiri! Ndipo anati wina ndi mnzace, 'Uyu ndani nanga? Ngakhale mphepo ndi nyanja zimvera Iye!'
Kulibe wina aliyense amene anakhoza kuletsa mphepo kuomba ndi mafunde kuwaza madzi!

**Kukambirana**
1. Ndi cifukwa ciani ophunzira a Yesu anaopa?
2. Kodi Yesu analetsa bwanji mphepo ndi nyanja?
3. Kodi masiku ano mphepo ndi nyanja zimvera Yesu?
4. Ndi cifukwa ciani zonse zimvera Yesu?
5. Kodi citanthauza ciani kwa inu kuti Yesu ndi Mbuye wa zonse?
6. Ngati ndife ana a Mulungu, kulibe ciriconse cimene cingatibvutitse koma cabe cimene Mulungu alola. Kodi ana a Mulungu ayenera kuopa zimene ziri kucitika m'miyoyo yao?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Mulungu wamphamvu zonse, Munasamalira ophunzira anu pamene anakuitani m'mabvuto ao. Mudziwanso mabvuto athu. Tikupemphani kuti mutithandize mwa cisomo, cifukwa Inu ndinu Wamphamvuyonse. Tithandizeni kukhala pafupi nanu ndi kukhulupirira kuti mulamulira zonse. Mwa Yesu Kristu Mbuye ndi Mpulumutsi tapempha izi. Amen.

## 5. Yesu analetsa matenda ndi imfa

*Ndipo mantha anagwira onsewo: ndipo analemekeza Mulungu, nanena kuti, Mneneri wamkuru wauka mwa ife; ndipo Mulungu wadzaceza ndi anthu ace – Luka 7.16*

**Kuwerenga**
Luka 8.49-56

**Malongosoledwe**
Yesu anati kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu. Anauza anthu kuti adacokera kwa Mulungu. Kenaka anacita zodabwitsa kuonetsa anthu kuti Iye atumidwa ndi Mulungu.
Pamene analetsa mphepo ndi nyanja, anaonetsa anthu kuti atumidwa ndi Mulungu. Anawaonetsa tero pociritsa anthu odwala. Ngakhale imfa inamumvera.
Dokotala akhoza kuthandiza anthu odwala. Angawapatse mankhwala. Koma sakhoza kuciritsa anthu. Ndi Mulungu yekha amene akhoza kuciritsa anthu odwala. Ndipo Mulungu yekha akhoza kuukitsa anthu akufa. Yesu anakhoza kucita zimenezi cifukwa Iye ndi Mulungu.
Baibulo litiuza za mtsikana amene anadwala kwambiri. Yairo, tate wake, anaitana dokotala. Koma mankhwala a dokotala sanathandize. Iwo anaopa kuti mwana angafe. Kenaka tate wa mtsikana anapita kukapeza Yesu.
Pamene Yairo anapeza Yesu, anagwa pa mapazi ake nati, 'O conde, bwerani ku nyumba yanga mosacedwa. Mwana wamkazi wanga ali kufa!'
Kunali anthu ambiri ozungulira Yesu, ndiye Yesu sanakhoze kufulumira. Mkazi m'modzi anadwala. Anadza pafupi ndi Yesu nakhudza copfunda ca Yesu. Yesu anazindikira kuti mkaziyo anakhudza copfunda cake ndipo Iye anaima nalankhula naye.
Yairo anayenera kuyembekeza. Ndipo sanafune kuyembekeza. Mwana wamkazi wake anadwala kwambiri. Anadziwa kuti mwana wake anali pafupi kufa. Anafuna Yesu kuthamanga.
Kenaka munthu wa ku nyumba ya Yairo anabwera mofulumira. Iye anati, 'Mwacedwa kwambiri. Mwana wamkazi wanu wafa'. O, Yairo anamva cisoni kwambiri. Yesu akadafulumira, mwana wamkazi wake angakhale moyo!
Koma Yesu anati, 'Usaope. Khulupira kokha'. Si kucedwa, osati kwa Yesu. Yairo sanaganize kuti Yesu angathandize mwana wamkazi wake atamwalira.
Tsopano Yesu anapita ndi Yairo. Anapeza mtsikana wokhala pa bedi. Anthu m'nyumba analira. Mwana anali wakufa. Koma Yesu anagwira dzanja lake. Yesu anati, 'Mtsikana, uka!'Ndipo mtsikanayo anauka. Anakhalanso moyo! Ndipo anali bwino. Yesu anauza mai wake wa mtsikanayo kumpatsa mwana wake kanthu ka kudya.
Yesu ndi wodabwitsa. Iye ndi wamphamvu zonse, cifukwa Iye ndi Mulungu.
Pamene tadwala, tipempha Yesu. Iye akhoza kuticiritsa. Nthawi zina Iye saciritsa anthu odwala. Aliyense ali ndi nthawi ya imfa yake. Koma si bvuto lalikulu. Cifukwa ngati timkonda Yesu, tidzapita kwa Iye pamene timwalira ndi kukhala naye Kumwamba muyayaya. Ici ndi cimene Yesu analonjeza. Koma akhoza kuticiritsa ngati afuna tero. Ali ndi mphamvu, ngakhale kuposa matenda ndi imfa.
Yesu anacita zodabwitsa zina zambiri, monga mudziwa. Anafuna kuonetsa anthu kuti Mulungu anamtuma. Anafuna anthu kumkhulupirira ndi kulemekeza Mulungu.

**Kukambirana**
1. Ndi cifukwa ciani Yairo anapempha Yesu thandizo lake?
2. Nanga inu, mumacita ciani pamene mukomana ndi mabvuto?
3. Kodi mudziwa zozizwitsa zina zimene Yesu anacita?
4. Kodi citanthauza ciani kwa inu kuti Yesu ali ndi mphamvu yuposa matenda ndi imfa?
5. Ndi cifukwa ciani Yesu saciritsa anthu nthawi zina?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Yesu Kristu, M'Baibulo tiwerenga zodabwitsa zambiri zomwe munacita. Ndipo tidziwa Inu ndinu Mpulumutsi amene ali ndi mphamvu zonse. Mutikhululukire kuti nthawi zambiri tifunafuna thandizo lina, osati Inu nokha. Titumizireni Mzimu wanu Woyera kutitsogolera m'miyoyo yathu. Tikupemphani izi mwa cisono m'dzina lanu. Amen.

## 6. Yesu anakhulululukira macimo

*Wodala munthuyo wokhulululukidwa chimo lace – Salimo 32.1a*

**Kuwerenga**
Marko 2.1-12

**Malongosoledwe**
Yesu anacita zodabwitsa zambiri. Analetsa mphepo yaikulu kuomba. Anaciritsa anthu odwala ambiri. Anaukitsa ngakhale wakufa.
Kenaka anacita cozizwitsa koposa. Mverani nthano iyi.
Tsiku lina Yesu anali m'nyumba ya mnzace. Anthu ambiri anabwera kumuona. Anafuna kumvera zimene akamba. Ngakhale adokotala anzeru ndi akatswiri a za malamulo anabwera. Nyumba inali yodzala ndi anthu kotero kuti kunasowa malo a anthu ena ngakhale munthu m'modzi.
Anthu onse anamvera Yesu. Koma ndi phokoso lotani limene anamva? Linacokera pamwamba pao. Anayang'ana pamwamba kuona cimene cacitika. Ndipo pamwambapo anaona amuna anai oyang'ana pansi pa dzenje ya m'tsindwi.
'Cenjerani!' amuna anati. Anali ndi mphasa ndi zingwe zomangidwa pa mbali zake. Ndipo anayamba kutsitsa mphasa patsogolo pa Yesu. Inatsika pansi. Anthu anaipatsa malo. Kunali mwamuna wogona pa mphasa! 'Sitinakhoze kulowa pa khomo', m'modzi wa amuna anai ananena, 'ndiye taboola tsindwi kuti mwamunayo wodwala angakhale pafupi ndi Yesu.'
Koma Yesu poona wodwalayo anaona cinthu cimene anthu ena sakhoza kuona. Anaona kuti mtima wa mwamunayo anamva cisoni cifukwa ca macimo. Pamenepo Yesu ananena, 'Mwana, macimo ako akhululukidwa.'
O, anthu anadabwa kwambiri! Adokotala ndi akatswiri anadabwa koposa. Anaganiza, 'Yesu sangalankhule tero. Yesu ndi munthu waamba. Mulungu yekha akoza kukhulululukira macimo.' Iwo sanakhulupirire kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu.
Yesu anadziwa maganizo ao. Anati, 'Ndidzakuonetsani kuti Mwana wa munthu akhoza kukhulululukira macimo'. Kenaka anati kwa wodwalayo, 'Ndikuuza iwe, nyamuka, senza mphasa yako, numuke kwanu'. Wodwalayo anacita zimene Yesu adamuuza. Anauka. Sanamve kudwala ngakhale pang'ono. Anayalula mphasa napita kunyumba moimba. Anasangalala kwambiri kuti aciritsidwa, makamaka kuti macimo ake akhulululukidwa. Ndipo anthu onse analemekeza Mulungu, cifukwa ca zodabwitsa za Yesu.
Yesu akhoza kukhulululukira macimo athu, cifukwa Iye ndi Mwana wa Mulungu. Ngati timuuza kuti tikumva cisoni pa macimo athu ndipo tikampempha cikhulululukiro, adzatikhulululukira macimo athu onse. Ici cidzatikondweretsa. Tingakhale okondwera ngakhale tadwala, ngati tidziwa kuti macimo athu akhulululukidwa. Cifukwa ngati macimo athu akhulululukidwa, tidziwa kuti Mulungu atikonda.
Kukhulululukidwa ku macimo ndi kofunikira kuposa kuciritsidwa. Ndi kofunikira kuposa ngakhale kuukitsidwa kwa anthu akufa.

**Kukambirana**

1. Ndi cifukwa ciani amuna anai anapita kwa Yesu?
2. Kodi Yesu anati ciani kwa wodwala poyamba?
3. Nanga ife, tingapite bwanji kwa Yesu kumpempha cikhulululukiro?
4. Ndi ciani cimene ciri cofunikira koposa: kuciritsidwa ku matenda kapena kukhulululukidwa ku macimo?
5. Kodi munadzicepetsa pa maso a Mulungu ndi kumpempha cikhulululukiro?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wamkulu, Tikuyamikani kuti mukhoza ndi kufuna kukhulululukira macimo. Uchimo ndi woipa kwambiri. Komabe mufuna anthu ocimwa kubwera ndi kulandira cikhulululukiro mwa Yesu Kristu Mpulumutsi. Ndinu Mulungu wacifundo ndithu! Tithandizeni kukukondani tsiku ndi tsiku. Mwa Yesu Kristu takupemphani izi. Amen.

## 7. Yesu anaonetsa m'mene aliri

*Yesu ananena kwa iye, Cifukwa wandiona Ine, wakhulupira; odala iwo akukhulupira, angakhale sanaona – Yohane 20.29*

**Kuwerenga**
Yohane 20.24-29

**Malongosoledwe**
Kodi mukumbukira zimene ophunzira a Yesu ananena pamene Iye analetsa mphepo ndi mafunde? Iwo ananena, 'Uyu ndani?'
Yesu anacita zodabwitsa zina, ndiye anthu ambiri ananena, 'Uyu ndani?' Nthawi zonse kunalibe munthu wocita zozizwitsa monga Yesu: kuciritsa anthu odwala, kuciritsa akhungu, kuukitsa akufa ndiponso ngakhale kukhulululukira macimo!
Anthu ananena, 'Kodi Yesu acita bwanji zodabwitsa izo? Kodi Iye ndi yani?'
Yesu anali ndi ophunzira khumi ndi awiri amene ankayenda naye tsiku ndi tsiku. Iwo anamumvera pamene anawaphunzitsa za Mulungu.
Tsiku lina pamene Yesu anali yekha ndi ophunzira ake Iye ananena, 'Kodi anthu anena ciani pali Ine? Kodi aganiza kuti ndine yani?'
Ophunzira ananena, 'Anthu ena aganiza kuti ndinu Yohane Mbatizi amene akhalanso moyo atamwalira. Ena anena kuti ndinu Eliya, mneneri waukulu wa kale. Ena anena kuti ndinu mneneri wina.'
Pamenepo Yesu ananena, 'Nanga inu, mukamba ciani? Ndine yani?'
Simoni Petro anayankha mosacedwa. Anati, 'Inu ndinu Kristu, Mwana wa Mulungu wamoyo!'
Petro anadziwa. Kodi Petro anadziwa bwanji?
Petro adaona ndi maso ake zodabwitsa za Yesu. Ndipo anadziwa kuti Mwana wa Mulungu yekha akhoza kucita nchito zazikulu zotero.
Ndiponso Petro adamvera ndi makutu ake zonse zimene Yesu adauza za Mulungu. Kulibe munthu amene angadziwe zambiri zotere za Mulungu ndi Ufumu wa Kumwamba koma Mwana wa Mulungu yekha.
Komanso, Petro anadziwa cifukwa Mzimu Woyera anamuuza. Mzimu Woyera analankhula m'mtima wa Petro namuuza kuti Yesu ndi Kristu, Mwana wa Mulungu.
Nanga ife, tingadziwe bwanji kuti Yesu ndi yani?
Zimene Yesu anacita ndi kunena, zitionetsa kuti Iye ndi yani. Tiwerenga izi zonse m'Baibulo.
Ndipo ngati tikhulupirira Baibulo, Mzimu Woyera adzalankhula kwa mtima wathu kutiuza kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu. Potero tidzakhala otsimikiza kuti Iye ndi Mpulumutsi wathu.
Petro ndi ophunzira ena anaona nchito za Yesu ndiponso iwo anamva mau odabwitsa a Yesu. Ife sitikhoza kumuona Yesu. Koma tikhoza kuwerenga zonse za Iye m'Baibulo ndipo tingakhulupirire. Kotero tingakhale okondwera cimodzi-modzi monga ophunzira amene anaona Yesu tsiku ndi tsiku.

**Kukambirana**

1. Kodi Petro anadziwa bwanji kuti Yesu ndi yani?
2. Nanga ife, tidziwa bwanji kuti Yesu ndi yani?
3. Kodi mukumva bwanji podziwa kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu?
4. Yesu ngati Mwana wa Mulungu ali Mkhalapakati. Kodi Mkhalapakati amacita ciani?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Mulungu, Zikomo kwambiri kuti Yesu anadzibvumbulutsa kwa anthu. Petro ndi ophunzira onse anaona kuti Yesu ndi wodabwitsa. Mutiphunzitse kuti tizindikirenso kuti ndinu wodabwitsa. Mutitsogolere kuti tione ukulu wanu ndiponso kuti tidzipereka kwa Inu. Tikupemphani m'dzina la Yesu Kristu. Amen.

# 8. Yesu anaonetsa ulemerero wake

*Pakuti Mwana wa munthu adzabwera mu ulemerero wa Atate wace, pamodzi ndi angelo ace – Mateyu 16.27a*

**Kuwerenga**
Mateyu 17.1-8

**Malongosoledwe**
Tinaphunzira kale kuti Yesu anadza kucokera Kumwamba. Adakhala Kumwamba kale kale asanabwere pa dziko lapansi ngati Mwana.
Mwamba ndiwo wodzala ndi ulemerero. Kumwamba zonse ndi zowala, zoyenerera ndi zosangalala. Yesu Mwana wa Mulungu anali wolemekezeka Kumwamba. Pamene anabwera pa dziko lapansi, Iye anasiya ulemerero wonse. Anaoneka cimodzimodzi monga amuna ena. Kunalibe munthu amene angaone kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu.
Koma tsiku lina Yesu anaonetsa ulemerero wake, ulemerero wa Kumwamba, kwa ophunzira ake atatu.
Tsiku lomwelo Yesu anati kwa Petro, Yakobo ndi Yohane, 'Bwerani ndi Ine'. Ndipo anawatenga naye kunka pamwamba pa phiri lalitali.
Pamwamba pa phiri, Yesu anagwada pansi kupemphera. Ophunzira anagwadanso.
Pamenepo cinthu codabwitsa cinacitika. Nkhope ya Yesu inayamba kuwala monga dzuwa. Zobvala zake zinakhala zoyera mbu monga kuwala. Pamene ophunzira anatsegula maso ao, sanakhoze kumyang'ana.
Kenaka, mwadzidzidzi, anthu awiri anali pamodzi ndi Yesu. Iwonso anaoneka akuwala. Iwo anali Mose ndi Eliya. Adaacokera Kumwamba kukalankhula ndi Yesu.
Petro, Yakobo ndi Yohane anangoyembekeza. Sanaone kale kuwala kwakukulu kotere. Kuwala kwa m'Mwamba ndi ulemerero wa m'Mwamba.
Potsiriza Petro anati kwa Yesu, 'Ambuye, mungatilole kumanga misasa itatu kuti ife tonse tikhale pano?'
Koma pamene analankhula, mtambo wowala unafika pa iwo. Ndipo mau anati, 'Uyu ndiye Mwana wanga wokondedwa. Mverani Iye!'
Mau ao ndi a Mulungu!
Ophunzira anaopa kwambiri. Anagwa nkhope zao pansi. Sanalimbe mtima kuyang'ananso.
Kenaka Yesu anabwera nawakhudza. Anati, 'Musaope'.
Ophunzira atatu anayang'ana mozungulira. Mtambo udacoka. Mose ndi Eliya adacoka. Ndipo kunalibe ulemerero wakuwala wa Yesu.
'Tiyeni tsopano, titsike pa phiri', Yesu anati.
Patapita nthawi iyo, ophunzirawa atatu anauza ena za ulemerero wa Yesu umene adaona pa phiri. Ndipo nthano yalembedwa m'Baibulo. Ophunzirawa atatu sanaiwale konse ulemerero wa Kumwamba.
Pamene Yesu adzabweranso pa dziko, potsiriza pa dziko lapansi, anthu onse adzamuona m'ulemerero wake wodabwitsa.

**Kukambirana**
1. Kodi Yesu anaonetsa bwanji ulemerero wake?
2. Ndi cifukwa ciani ophunzira a Yesu anagwa nkhope zao pansi?
3. Kodi muopa ulemerero wa Mulungu?
4. Uchimo utsutsana ndi ulemerero wa Mulungu. Ndi cifukwa ciani macimo athu ayenera kucotsedwa tisanaloledwe Ufumu wa Mulungu?
5. Kodi tidzaona ulemerero wa Yesu pa nthawi yanji?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wolemekezeka, Ulemerero wanu ndi waukulu. Tikugwadirani modzicepetsa. Tikuyamikani kuti ndinu wamkulu ndi woyera. Mutikhululukire macimo athu onse kuti mudzatilola kukhala nanu m'ulemerero wanu Kumwamba. Tikuyembekezani kubweranso kuti tione ulemerero wanu. M'dzina la Yesu Kristu tapempha ndi kusiya izi. Amen.

**Sewero**

Pezani mau onse ndipo lembani yankho mogwiritsa nchito mau osaphedwa.

| | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| Y | O | H | A | N | E | N | D | I | N |
| E | P | M | K | R | I | S | T | U | G |
| S | E | K | U | M | W | A | M | B | A |
| U | H | I | W | D | N | I | S | T | L |
| Y | P | P | M | A | C | I | M | O | A |
| A | M | A | T | E | N | D | A | U | W |
| I | O | L | S | Y | A | N | I | O | A |
| R | Y | U | I | I | M | F | A | R | N |
| O | O | G | K | H | O | L | A | E | G |
| U | S | N | A | M | I | N | U | R | E |
| A | A | U | N | W | A | K | E | E | L |
| N | T | L | A | Y | I | R | A | M | O |
| A | A | U | A | N | T | H | U | E | U |
| W | N | M | P | E | T | R | O | L | T |
| M | A | F | U | N | D | E | S | U | I |

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| mphepo | matenda | Yesu | Yohane | ngalawa |
| Yairo | macimo | mtsikana | mafunde | ulemerero |
| angelo | moyo | khola | Kristu | Mariya |
| Kumwamba | Mwana | tsindwi | Petro | Satana |
| imfa | Mulungu | yani | anthu | wake |
| ndi | inu | | | |

Yankho:………………………………………………………………

**Nyimbo**

(Yesaya 45.22)

Yang'anani kwa Ine, mupulumutsidwe
Yang'anani kwa Ine, Yehova
(Ine ndine) Ine ndine Mulungu, palibe wina
Ine ndine Mulungu yekha.
(Onse) Onse
(Onse) Onse
a dziko, yang’anani
Yang'anani kwa Ine, mupulumutsidwe
Ine ndine Mulungu yekha.